WEEKEND NATION
LOWERUKA, OCTOBER 1, 2022



A Usi kuyendera zida za alenje

# Nduna yiyamikira wogwira ntchito kunkhalango ya Majete

WOLEMBA:
MARTIN GELA JNR

Nduna yazokopa alendo, chikhalidwe ndi nyama zakutchire a Micheal Usi ayamikira wogwira ntchito kunkhalango ya Majete ponena kuti akuzipereka kwambiri.

Iwo adati ogwira ntchito kumalowa kuyambira akuluakulu mpaka achinyamata ndi amwambo zomwe zimachititsa kuti akauzana nthawi yogwira ntchito azikumana m'nthawi yake motsutsana ndi momwe wogwira ntchito ena munthambi zina zaboma akugwilira ntchito zawo.

"Nthawi yakwana kuti onse aulesi komanso sachita zomwe malamulo a ntchito akufuna achotsedwe ndi kuika okhawo omwe ali ndi kuthekera kogwira ntchito kuti masomphenya a chitukuko a boma a Malawi 2063 akwaniritsidweadatero a Usi.



ZITHUNZI: MARTIN GELA

Asilikali a nkhalango ndi mfuti zawo

Pantchito ya Shire Valley Transformation Programme yomwe amayendera iwo adati ngalande za ntchitoyi zikudutsa m'nkhalango zawo kotero anayenera kuti agwirire limodzi ndi unduna wa zaulimi ndi cholinga chofuna kuteteza mtsinje wa Shire komanso nyama za m'nkhakangozi.

Ndunayi idati ichi n'chifukwa chake ndi ndalama zokwana $5.6 miliyoni kuchokera ku Global Environment Facility (GEF) nthambi ya za m'nkhalango yayambitsa ntchito zotukula miyoyo ya anthu omwe amakhala mozungulira nkhalango za Majete, Lengwe, Mwabvi komanso Matandwe ngati kuwapatsa mbuzi zomwe adzipatsirana zisanu pabanja linalilonse zinayi zazikazi ndi toned mmodzi komanso kuwaphunzitsa kuweta njuchi zomwe ziziwapatsa uchi.

Iwo anati kupyolera kuntchitozi anthu akusiya kupanga ntchito zoononga mitengo ngati kuotcha makala, kucheka matabwa komanso kupha nyama m'nkhalangozi.

Mtsogoleri woyang'anira zachitetezo kunkhalango ya Majete a Martin Wazi anadandaula ndi mchitidwe wokupha nyama mosavomerezeka.

A Wazi adati "Takhazikitsa gawo lina lachitetezo la agalu lomwe tikulitcha kuti K9 Unit, omwe amafufuza alenje omwe akumapha nyama pogwiritsa ntchito zinthu monga zigwenembe, mawaya komanso mfuti zagogodera zomwe panopa tinalandapo zoposa 500."

Iwo adati kupatula kupha nyama alenjewa anapha mmodzi wa iwo atakodwa pamsampha wa chigwenembe ndipo anamutsiriza ndi nkhwangwa.

Nkhalango ya Majete yomwe kukula kwake ndi masikweya kilomita 700 anayiika m'kaundula wa boma m'chaka cha 1955 ndipo inatengedwa ndi a African Parks pa 28 March 2003, nthawiyo anthu atatu ndi omwe amabwera kudzaona nkhalangoyi koma pano zikuonetsa kuti anthu woposa 9 000 ndiwo amabwera kudzaona malowa.

Nkhalango ya Majete ili ndi nyama zokwa 12 500 malingana ndi chiwerengero cha nyama chomwe chinachitika mu 2020. Mwazina mwa nyamazi ndi nswala 27, mikango 45, mimbulu 15 komanso njobvu pakati pa 350 mpaka 400. ■

## BWALO LA ULIMI



WOLEMBA: ANDREW SAUKANI

# Sadc pamgwirizano wa nsomba

M'chaka cha 2000 maiko a m'bungwe la Sadc anagwirizana zokhazikitsa ndondomeko za kayendetsedwe ka chitukuko chausodzi ndi ulimi wa nsomba yotchedwa Sadc Protocol on Fisheries.

Ndondomekoyi inasanjidwa ndi nsanamira kapena kuti magawo 29 zimene zatsindika m'magawo osiyanasiyana a mmene maikowa akufunira kuti chitukuko cha usodzi ndi ulimi wa nsomba chiyenera kuyendera.

Maiko a m'bungweli sakukakamizika kutsatira nsamamirazi koma dziko palokha likaunikira ngati ndondomekozi zili zothandiza ndipo litha kuchitapo kanthu, lili ndi ufulu wosainira nawo mgwirizanowu.

Ndi maiko 14 okha kuphatikizapo Malawi ndi amene anasayinira ndi kuvomereza panganoli. Chimene tiyenera kudziwa n'choti maiko a m'chigwo cha SADC akukhudzidwa mosiyanasiyana pankhani za usodzi ndi ulimi wa nsomba chifukwa ena ali ndi nyanja za mchere, ena ali ndi nyanja zokha mkati mwawo zimene zina mwa izo ndi zogawana pakati pa maiko angapo komanso ena ali ndi mitsinje yambiri mkati mwao imene akumachitirako usodzi ndi ulimi wa nsomba.

Lisanakhazikitsidwe pangano la Sadc Protocol on Fisheries, dziko la Malawi ndi limene linkalumikizitsa pa ntchito zoyan'ganira ulimi wa nsomba ndi usodzi wa mkati mwa nyanja za m'maiko a m'chigawo cha Sadc pamene dziko la Namibia linkalumikizitsa ntchito za usodzi m'nyanja za mchere.

Pofuna kuonetsetsa kuti ntchito za usodzi zikulandira chidwi ndi thandizo loyenera, bungwe la Sadc linakhazikitsa nthambi yapaderadera yoyan'ganira usodzi yotchedwa Fisheries Division. Motsatana ndi gawo 5, lamulo 21, la bungwe la Sadc, maiko akulimbikitsidwa kugwirana manja poteteza ndi kutukula ntchito za usodzi.

Cholinga cha Sadc Protocol on Fisheries ndi kulimbikitsa maiko kusamala ndi kugwiritsa bwino zachilengedwe zopezeka m'nyanja ndi m'mitsinje yawo mokomera nzika zawo komanso kupindula pantchito zachuma.

Maiko amene anasainira ndi kuvomereza ndomekozi akuyenera kuonetsetsa kuti zachilengedwe za m'madzi zikuthandizira pa kapezedwe ka chakudya, kukweza thanzi la anthu awo nsomba zikupindulira anthu ndi kukweza chuma m'maiko awo.

Kuti izi zikwaniritsidwe, nsomba zikuyenera kumaphedwa motsata njira zabwino zosasakaza chilengedwe koma pamlingo oti zikathe kuchulukananso mosavuta. Maiko a m'bungwe la Sadc ili ndi kuthekera kwambiri pa ulimi wa nsomba chifukwa madera onse ali ndi zonse zofunikira pa ulimi wa nsomba koma kungoti vuto ndi kusowekera kwa ukadaulo, luso ndi ndalama zokuziriza ntchitoyi.

Nthawi zina maiko alibe malamulo okhwima oteteza usodzi maka pamene wina aliyense ali ndi ofulu opha nsomba m'mene angafunire. Maiko amu Sadc ali ndi msika waukulu kwambiri pa malonda a nsomba chifukwa chiwerengero cha anthu n'chokwera kwambiri.

Sizoyenera kuti anthu a m'chigawo cha SADC azinyentchera kaamba kosowa zakudya monga nsomba pemane azunguliridwa ndi Nyanja komanso mitsinje yochuluka. ■

Mafunso: saukaniandrew@gmail.com